اللغة التشيشيوا

CHICHEWA

دليل المسلم الجديد، ما هو الإسلام؟

للشيخ د. هيثم سرحان

# MLONDOLI WA ONGOLOWA KUMENE CHISILAMU



DR.HAYTHAM SARIHAN

# NDINGALOWE BWANJI CHISILAMU?

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| Kodi kulowa chisilamu ndikophweka? | Eya kulowa chisilamu ndikophweka chifukwa sizimasaukila mkhala pakati. |
| Kodi ndikuyenera kuchita changu kulowa chisilamu? kapena ndikuyenera kudikila nthawi yoyenera? kapena ndikuyenera kuthetsa kaye ena mwa mavuto? | Ndizoyenera kuchita changu kulowa chisilamu, chifukwa kuchedwetsa kulowa chisilamu kukhoza kubweresa chionongeko, utha kumwalira nthawi iliyonse, ngati mmene zilili kuti kulowa chisilamu ndi Geni(bizinesi yopindula), choncho nthawi iliyonse imene munthu akuchita changu kupita ku geni phindu lake limakhala lochuluka. |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| Achite chani munthu amene akufuna kulowa chisilamu? | Zimangofunika basi kungoyankhula ma shahada awiri: ((Ndikuiikila umboni kuti palibe wina oyenera kumpembedza mwachoonadi kupatula Allah yekha, ndikuikilanso umboni kuti Muhammad ndi kapolo wake komanso mtumiki wake)). |
| Shahadayo ayankhule mu chilankhulo changu? | Akhoza kuyankhula chilankhulo chilichonse chimene amakwanitsa bwino,ndipo sizili zokakamiza kuyankhula mu chiluya(charabu). |
| Kodi atha kuyankhula shahadayo ngakhale asakumva matanthauzo ake? | Ayi ndizosatheka,ndi zoyenera kuti amve kaye matanthauzo ake ndikuzikhulupilila zomwe zili mkati mwakemo, komanso |

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| | kuzigwiritsa ntchito zomwe zikukamba shahadayo. |
| Mawu akuti "ashahadu" amatanthauza chani? | Kutanthauza kuti: ndikuvomereza ndi mtima wanga,ndipo ndikuyankhula ndi lilime langa,ndi kugwira ntchito ndi ziwalo zanga. |
| Mawu akuti "Lã ilãha illallãhu" akutanthauza chani? | Amatanthauza kuti: Palibe wina opembedzedwa mwa choonadi kupatula Allah yekha. |
| Mawu akuti: "Anna Muhammadan abduhu warasūluhu"(Muhammad ndi kapolo wake komanso mtumiki wake)akutanthauza chani? | Akutanthauza kuti: Ameneyo ndi kapolo sapembedzedwa, komanso ndi Mtumiki satsutsidwa.<br><br>Ndipo zikukakamizika ndi shahada imeneyi:kumuvomereza zimene wafotokoza,kumumvera pa zimene walamula,ndi |

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| | kuzisiya zonse zomwe waletsa, komanso kutsatira chiphunzitso chake ndikumutenga kukhala chitsanzo chako. |
| Ndamvetsa bwino kwambiri. | Ukuyenera kubwereza pambuyo panga mawu awa: |
| Ndi chani chimene chikufunika tsopano kuti ndipange? | "Ndikuikila umboni kuti palibe wina oyenera kumpembedza mwachoonadi kupatula Allah yekha, ndikuikilanso umboni kuti Muhammad ndi kapolo wake komanso mtumiki wake ". |
| Kodi pamenepa tsopano ndine Msilamu? | ◌́Eya, ndipo Allah atamandike. Umenewu ndi ubwino wa Allah pa iweyo pokuika kukhala Msilamu tsopano. |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| Tsopano ndi chani chomwe mungandilangize ineyo ngati Msilamu? | ̧Ndikukulangiza zochulukitsa kumupempha Allah kuti akulimbitse pa chipembedzo chake, komanso ukuyenera uzisankha anzako abwino oyenda nawo amene angakuthandizire pa chipembedzo chako, komanso ukuyenera kuchiphunzira chisilamu, ndikupanga mobisa chisilamu chako mpakana chitalimba ndikukhazikika muchifuniro cha Allah. |
| Pempho labwino kwambiri ndi liti? | ))Tiongoleni ife ku njira yolungama)) [Alfãtiha:6]. |
| Kumkumbukila Allah (dhikiri) kopepuka ndi kuti? | Dhikiri yopepuka kwambiri ndi {Bismillah},imanenedwa pomwe tikulowa mu mzikiti ndi mnyumba, komanso |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| | pomwe tikuluka mmalo awiriwa, tikamafuna kuwerenga Quran, tisanalowe mchimbuzi, tisanayambe sanayambe kuvula zovala,tisanayambe kupanga udhu, tisanayambe kudya ndi kumwa, ndi malo ena ochuluka osakhala amene atchulidwawa. |
| Malamulo akuti chani za machimo omwe ndinapanga ndisanabwelere ku chisilamu? | Chisilamu chimagula ndi kufufuta zonse za m'mbuyo mwake kumbali ya machimo, kupatula ma ufulu a anthu ena omwe ali okakamizika kubweza, izi zimakakamizika kuwabwezera eni ake. |
| Pambuyo pakuti ndapanga shahada,ndi chani chimene chikufunika kuti ndipange? | Ukukakamizika kuti usambe. |

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| Ndisambe chifukwa chani? | Choyamba: ukuyenera kudziwa kuti: Msilamu sayenera kunena kuti "chifukwa chani ndipange zimenezo?" Koma amayenera kuyankhula kuti {{Tamva ndipo titsatira}} [alnoor:51].<br><br>Chachiwiri: ukuyenera kusamba kuti uyeretse panja pa thupi lako, ngati mmene wayeretsera mkati mwako. |
| Chabwino, ndiye ndingasambe bwanji? | Utsimikize mu mtima mwako zosamba, kenako unene kuti "Bismillah", kenako uthile madzi thupi lako lonse. |
| Ndi chani chimene chikutsatira pambuyo pakusamba? | Ikakwana nthawi ya swala, ndiye kuti ukuyenera kuswali kudzera mu chifuniro cha Allah. |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| Swala ingandivute, chifukwa mmenemo muli zoyankhula komanso zochita zimene ine sindimatha. | Chisilamu ndi chipembedzo chofewa,si chipembedzo chokhwima ayi, ndipo Allah atamandike pa zimenezi. |
| Ndiye ndingaswali bwanji? | Ukuyenera kutsatira swala limodzi ndi ine(pambuyo panga), kapena uonele tima kanema(video) tophunzitsa kwasalidwe,ndipo tima video timeneto tili mu zilankhulo zochuluka, tikupezekera mu chanelo cha MAÃHAD ALSUNNAH kudzera mu ma linki omwe ali ku mapeto kwa uthenga umenewu. |
| Ndi chaninso china pambuyo pa swala? | Ukuyenera kuphunzira nsichi zisanu zomwe zikumanga chisilamu, kenako nsichi za chikhulupiliro, choncho ... |

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| | Kufikila umalize kuphunzira zonse zomwe zingakhoze usilamu wako ndi chikhulupiliro chako(imaan). |
| Ndi ma samba ati a mchezo omwe mungandilangize ine kuti ndilowe? | Ndikukulangiza zotsatira ma samba kapena ma chanelo a maulama akulu akulu komanso ma bungwe a Dawa omwe akupezeka mu dziko la Saudi Arabia. |
| Ndingakhale bwanji ndi azibale anga omwe sali asilamu? | Uzikhala nawo ndi kuchita nawo zinthu limodzi ngati mmene Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye amachitira ndi omwe sanali asilamu. Iye anali oyitanira ku chisilamu pogwiritsa ntchito lilime lake,khalidwe lake ndi machitidwe ake a zinthu. |

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| Pali yemwe akufuna kulowa chisilamu,koma sakufuna kuwadziwitsa akubanja kwake, malamulo akuti chani pa zimenezi? | Sizokakamizika kwa aliyense amene walo chisilamu kumudziwitsa munthu wina, chisilamu chimakhala pakati pa iyeyo ndi Allah. |
| Ndi buku liti lomwe lili labwino kwambiri mu chisilamu? | Buku labwino kwambiri ndi Quran yolemekezeka,omwe ndi mawu a Allah wapamwambamwamba. |
| Ndi surah iti yofunika kwambiri mu Quran yolemekezeka? | Surah yofunika kwambiri mu Quran yolemekezeka ndi surat Alfãtiha, ndi chifukwa chake timaiwerenga mu rakat iliyonse pa swala. |
| Ndi Ayah iti imene ili yaikulu kwambiri mu Quran yolemekezeka? | Ayah imene ili yaikulu kwambiri mu Quran yolemekezeka ndi ayatul Kursiyy. |
| Ndingakwanitse bwanji kuwerenga Quran? | Kudzera mu njira yoiphunzira Quran yo, komanso kumvelera |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| | mawerengedwe amasheikh,monga kuwerenga kwa sheikh Hudhaifa, Alhuswair ndi ma sheikh ena. |
| Ndingaimvetse bwanji Quran? | Ukhoza kuimvetsa bwino powerenga ma buku a tafseer omwe analembedwa ndi maulama odziwika bwino. |
| Ndingapeze kuti ma buku a tafseer? | Utha kupezeka tafseer ku bungwe lomwe limalemba ma Quran lomwe likupezeka ku Madina. |
| Nanga ndi chaninso chimene mungandilangize kuti ndiziwerenga pambuyo pa Quran? | Ndikukulangiza zowerenga ma Hadith olondola a Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye. |
| Ndi buku liti lomwe lili labwino kwambiri la ma | Buku labwino kwambiri komanso lolondola la ma Hadith a Mtumiki ndi |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| Hadith a Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye? | (Swahih Bukhar ), anthu anagwirizana za buku limeneli ndipo anasangalatsidwa nalo ma ulama akulu akulu , komanso ndikukulangiza za link yopangila daunilodi ma buku yomwe ili kumapeto kwa uthengawu. |
| Ndi Hadith iti yofunika kwambiri mu chiphunzitso cha Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye? | Hadith ya Jibril yomwe anabwera kudzalongosola za ma gawo atatu a chisilamu (steps): chisilamu, chikhulupiliro ndi ubwino. |
| Ine ndikuopa kuti sindingakwanitse kuchiphunzira chisilamu. | Osaoa; zomwe ukuyenera kuchita ndikuyezamira mwa Allah, ndipo Allah akuthandizira mu njira yako yophunzira chisilamu, chipembedzo ndi chofewa. Allah akupatse chiyanjo ku |

| Funso | Yankho: |
|---|---|
| | zomwe amazikonda ndi kusangalatsidwa nazo.<br><br>Ndipo ndi zotheka utha kumaphunzira nafe ONLINE mwa ulele ku mãhad yathu MÃHAD ALSUNNAH pa ma link omwe ali ku mapeto kwa uthengawu.<br><br>Pomaliza,ndikukulangiza za kuyankhula kwa Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye:"udziikila chidwi pa zinthu zimene zingakuthandize ndipo uziyedzamila mwa Allah ukafuna kuchita chinthu,ndipo osataya |

| Funso | Yankho: |
| --- | --- |
| | mtima ndi kufooka pa kalikonse". |

# MA LINK AKU MAÃHAD ALSUNNAH:

Telegram

Facebook:

Portal ya maãhad alsunnah:

Whatsapp

Twitter (X):

Instagram:

Kupanga daunilodi ma buku :

YouTube:

# 3 MITUNDU YA TAUHEED

Kumupatula Allah (olemekezeka) muzinthu zimene wapatulika nazo, kumbali ya umbuye,umulungu ndi maina komanso mbiri zake.

NDIPO MITUNDU YAKE ILIPO ITATU:

### Tauheed ya maina komanso mbiri za Allah (al-Asmãu wa swifat)

Uku ndiko kumupatula Allah pa maina omwe wazitchulira yekha kapena mbiri zomwe wazifotokoza yekha mu buku lake la Quran, kapena kudzera pa lilime la Mtumiki wake mtendere ndi madalitso zipite kwa iye.Kumupatulaku kwagona potsindika zomwe iye mwini watsindika, ndikuzikana/kuzitsutsa zomwe mwini wake azitsutsa, mopanda kusintha kapena kuchotsa mbiri zonse kapena zina mu mbiri za Allah,mopandanso kunena kuti mbiri zakezo zili bwanji(mwachitsanzo kunena kuti:ngati wakhala wakhala motani?), komanso mopanda kufanizila ndi mbiri za zolengedwa zake.

### Tauheed ya umulungu (al-uluhiyyah)

Uku ndiko kumupatula Allah pompembedza, kapena pa zintchito za akapolo.

### Tauheed ya umbuye (al-rububiyyah)

Kumeneko ndiko kumupatula Allah pa zintchito zake, kapena kumupatula Allah pa kulenga, umwini pa chilichonse ndi kuyendetsa zinthu.

## Ndondomeko(mndandanda) wa chipembedzo uli mmagulu atatu:

### AL IHSAN(UBWINO)

Kumupembedza Allah ngati ukumuona, ngati zili zakuti siukumuona ndiye udzindikire kuti iyeyo akukuona.

**Nsichi imodzi pansi pake pali ndondomeko/ ma sitepe awiri:**

1-mapemphero akuona: Umpembedze Allah ngati ukumuona.
2-mapemphero akuyang'anilidwa: Ngati siukumuona zindikira kuti iyeyo akukuona.

### AL IMAN (CHIKHULUPILIRO)

Uku ndiye kuyankhula ndi lilime ndi Kutsimikiza ndi mtima,kugwira ntchito kudzera mu ziwalo. Chikhulupiliro chimaonjezereka komanso chimapunguka.

**NSICHI ZA CHIKHULUPILIRO: 6**

1-Kukhulupilila mwa Allah.
2-Mwa Angelo ake.
3-Mabuku ake.
4-Atumiki ake.
5-Za tsiku lomaliza.
6-Ndi kukhulupilila za chikhozero chabwino ndi choipa kuti zonsezo zimachokera kwa Allah.

### AL ISLAM (CHISILAMU)

Kumeneko ndi kuzipeleka mwa Allah pomupatula,ndi kugonjera mwa iye pomumvera, komanso kuzitalikitsa ku shiriki ndi anthu opanga za shiriki wo.

**NSICHI ZA CHISILAMU: 5**

1-Ma shahada awiri.
2-Kuimika swala.
3-Kupeleka chaulele(zakah).
4-kusala kudya(swaum) mmwezi wa Ramadhani.
5-Kukapanga Hajj ku nyumba yolemekezeka,kwa yemwe ali ndi kuthekela kokafika kunyumbayi.

## 4 MAGULU AZINTHU ZOLETSEDWA (HARAM)

### MACHIMO ANG'ONO ANG'ONO

Awa ndi machimo omwe sanafike mulingo wa machimo akulu akulu. Machimo akulu akuluamachotsedwa (kufufutidwa)popempha chikhululuko ndipo machimo ang'ono ang'ono amasanduka kukhala akulu akulu ngati munthu akupitilira kuwapanga panga, Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye adati: "Atalikileni machimo ooneka monyozeka (ang'ono ang'ono) chifukwa machimo amenewo amasonkhana mwa munthu kufikila kuti amadzamuononga munthuyo".

### MACHIMO AKULU AKULU

Chilichonse chimene chalumikizidwa ndi chilango chopatulika pa tchimo limenelo. Machimo amenewa ndi monga: Ufiti,Kunyoza makolo awiri, katapila,Chigololo,kugonana amuna kapena akazi okha okha, bodza, kumwa mowa, kuba, miseche,kupha munthu popanda chifukwa chovomerezeka ndi sharia, komanso kudya chuma cha ana a masiye.

### Shiriki yaing'ono

Mtundu uwu wa shiriki siumtulutsa munthu mu chipembedzo,koma kuti ndi tchimo lalikulu m'machimo omwe ali akulu akulu.Mwachitsanzo ngati kuyankhula kuti : izi ndi zomwe wafuna Allah ndi iweyo (maa Shaa Allah wa shiita), kulumbila mosakhala mwa Allah, kuzionetsera kwakung'ono (riyah yaing'ono)kupachika zithumwa,kudziwa mwayi kapena tsoka kuchokera mu mbalame, ndi zinthu zina zochuluka zimene munthu angazipange kukhala zida zozitetezera kapena kuti zimenezo zitha kumuteteza ku ufiti.

### Shiriki yaikulu

Iyi imamutulutsa munthu mu chipembedzo,ndipo samakhululukidwa ngati wamwalira ali pa shiriki yo. Wa shiriki yaikulu amamuikila Allah timilungu tina ndikumatipembedza kapena kutipempha ngati mmene amamupemphera Allah, kapena amalakalaka kena kake kuchokera ku timilungu timeneto kapena kutikonda ngati m'mene angamukondele Allah, kapena amakhala akutipangila mtundu wina wake wa mapemphero .

# ZAKATI ILI MMAGULU AWIRI

**1-YA SUNNAH:** Ndipo ichi ndi chuma chilichonse chimene munthu amapeleka mu njira ya ibadah (kumpembedza Mulungu).

**2-YA FARADH (YOKAKAMIZIKA)**

Iyi ili mmagulu awiri:

## ZAKATI YA ZAKUDYA:

Iyi ndi imene imatchedwa kuti Zakatul fitir, imene imapelekedwa ku mapeto kwa mwezi wa Ramadhani, ndipo ndiyokakamizika kwa msilamu aliyense, wamkulu,wamng'ono, wammuna kapena wamkazi,kapolo kapena mfulu.

## ZAKATI YA CHUMA (NDALAMA):

Tanthauzo lake pa sharia:uku ndi kumpembedza Allah popeleka gawo lomwe lili lokakamizika pa sharia kuchokera mu chuma chodziwika bwino,chumacho chipite ku kagulu kapena mbali yodziwika bwino.Ndipo imeneyi ndi msichi yachitatu mu msichi za chisilamu.


Zakati imeneyi ili mmagulu anayi(4).

### 1 NDALAMA ZIWIRI



Golide ndi Siliva kumpatikizaponso mtundu ulionse wa ndalama (ngati ma kwacha).Golide mulingo wake ndi 20(omwe ndi ma galamuzi 85).
Pomwe mulingo wa Siliva ndi 200 (omwe ndi ma galamuzi okwana 595).

### 2 ZIWETO



Zimene gawo lalikulu pa chaka zimadyetsedya ndi msipu waulele. Ndipo ziweto zake ndi monga: Ngamila, Ng'ombe, Mbuzi kapena Nkhosa.

### 3 ZOTULUKA MU NTHAKA



Izi ndi Njere (monga chimanga) Ndi Zipatso (monga tende)

### 4 CHUMA CHA MALONDA



Ichi ndi chilichonse chimene chaikidwa pa mndandanda wa kugula ndi kugulitsa(bizinesi).

## ENI ZAKATI (OYENERA KULANDILA)

**OVUTIKITSITSA (MA FUQARAU) 1**
Awa ndi ovutika omwe sapeza kalikonse, kapena amapeza zowakwanira zochepa kwambiri pa moyo wawo.

**OSAUKA (MISIKINI) 2**
Awa ndi omwe amapezako zowathandiza zochulukilapo kapena theka pa Chaka.Titati tiyelekeze kuti ndalama imene ingakwanire kudya pa chaka ndi K12000.Ovutika aja ndiye kuti akhala ndi K6000, kapena alibiletu.Pomwe osaukawa ndiye kuti akhala ali ndi K6000 kapena kuposela pamenepo, koma safika pa K12000. Choncho ife timayenera kumpatsa ovutika ndi osauka yu chimene chingawakwanire pa chaka.Zili choncho chifukwa zakati imakakamizidwa chaka chikazungulila.

**OGWIRA NTCHITO YA ZAKATI: 3**
Awa ndi omwe amatolera,kusunga ndi kugawa zakati.Ntchito imeneyi amapatsidwa ndi mtsogoleli. Awa amapasidwa zakati osayang'ana kuti ndi osauka kapena olemela.ngakhale ali olemela amayenerabe kuti apatsidwe zakah.

**OFEWETSEDWA MITIMA YAYO 4**
Awa ndi omwe timayembekezera kuti atha kulowa chisilamu, kapena kusiya kwavutitsa asilamu(ngati atsogoleli adera) kapena omwe tikufuna kuwalimbikitsa chikhulupiliro chawo(imaan).

**AKAPOLO 5**
Awa ndi:A- Msilamu yemwe walembeledwa kuti ngati atapeleka ndalama mwakuti basi amasulidwa ukapolo.B- Kummasula ukapolo msilamu. C- Msilamu yemwe wagwidwa ukapolo ku nkhondo.

**OTHINIDWA NDI NGONGOLE 6**
Awa ndi:A-Yemwe wagwa mu ngongole chifukwa chofuna kuyanjanitsa anthu omwe asemphana.B- Yemwe wagwa mu ngongole chifukwa chofuna kuzithandiza pa mavuto ake omwe anamugwera.

**YEMWE ALI PA NJIRA YA ALLAH 7**
Umu mukulowa asilikali a nkhondo ndi kalikonse kamene angasaukile monga zida ndi zina zotero.

**WA PAULENDO 8**
Uyu ndi munthu yemwe wauyamba ulendo ndipo kamba wake wa pa ulendo watha (monga tarasipoti), choncho amapasidwa zokamufikisa kwawo komwe wachokera kapena komwe akulowera.

Chichewa التشيشيوا

# SWAUM(KUSALA) ILI MMAGULU AWIRI

**YA SUNNAH:** Iyi ndi yomwe imachitika posakhala nthawi zitatuzi.

**YOKAKAMIZIKA (WAJIBU):** Iyi ndi yomwe imachitika mmwezi wa Ramadhani, ina ndi ya Dipo(kaffarah) ndi ya Lonjezo(nadhir).

**TANTHAUZO LA SWAUM (KUSALA):** Uku ndiko kumpembedza Allah posiya kudya, kumwa ndi kena kalikonse komasulisa.Zimenezi kuyambila kutuluka kwa fajiri yoona kufikila kulowa kwa dzuwa.

## SWAUM ILI NDI MSANAMILA ZIWIRI

### 1 CHITSIMIKIZO (NIYAH)

| NIYAH YA KUSALA KWA SUNNAH | NIYAH YA KUSALA KWA FARADH |
|---|---|
| Ndi zotheka kupanga niyah nthawi iliyonse dzuwa litatuluka ngati munthu sanapange kalikonse komasulisa swaum (monga kudya), Munthu ameneyu amapeza malipilo akusala kuyambila pamene wapangila niyah. | Kusala uku zimakakamizika kupanga niyah (Chitsimikizo usiku nthawi ya fajiri iasanakwane.ndipo zimakwanira kupanga niya ya kusalaku kumayambililo kwa mwezi kuti usala mwezi onse wa Ramadhani.Niya malo ake ndi muntima ndipo kuyankhula pa lilime ndi bidia zopeka. |

### 2 Kuzisiya zomasulitsa swaum.



**ZOONONGA SWAUM (KUSALA):**

1-kudya kapena kumwa mwadala, choncho amene wadya moiwala swaum yake ndi yabwino bwino.
2-Kugona ndi mkazi kapena mwamuna:izi zikachitika usana wa mwezi wa Ramadhani,ndipo ochitayo nakhala kuti swaum ndi YOKAKAMIZIKA pa iyeyo, ndiye kuti adzayenera kupeleka dipo lokhwima kwambiri
3-kutulutsa umuna kapena ukazi. 4-Kalikonse kamene kangalowe mu gulu la kudya kapena kumwa, monga jakisoni wa zakudya. 5-Kutulutsa magazi munjira yozichiza (cupping) 6-kusanza mwadala 7-Kutuluka magazi akumwezi( piriodi) kapena aubeleki (nifasi).

**ZINA MWA ZOLOLEDWA KWA OSALA:**

- Kulawa chakudya.
- Kumeza malovu.
- Kusamba.
- Kutsuka mkamwa ndi mswachi.
- Kuzinunkhiritsa.
- Kuziziziritsa .

## ZOMWE ZIMAPANGITSA KUTI SWAUM IKHALE YOKAKAMIZIKA:

1-Kukhala Msilamu.

2-Nzeru.

3-Kutha msinkhu.pomwe osatha msinkhu ndiye angolimbikisidwa zosala ndipo omuyang'anira wake azimulamula zakusala

4-Kukhala ndi kuthekela kosala:Kusala sikukakamizika kwa munthu wa pa ulendo,koma zabwino ndiye kusalako ngati akuona kuti sizimupatsa mavuto.zili choncho chifukwa mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye adayamba wasalako ali pa ulendo.Komanso munthu umamasuka mwachangu,ndipo ndi zopepuka kwa munthu yemwe akulamulidwa zakusala,ndipo amapeza nawo ma ubwino akusala mmwezi wa Ramadhani.

5-Kukhala ndi umoyo wa thanzi.

6-Kusadwala kumwezi kapena matenda aubeleki

**ZIMALETSEDWA KWA MUNTHU OSALA:**

1-Kumeza malovu kapena makhololo koma sizimasulisa swaum 2-Kuphsyophsyonana milomo kwa omwe akuopa kuti atha kuononga swaum yawo.3-Kutankhula bodza komanso kupanga kalikonse ka haram. 4-Umbuli 5-Kulumikiza( osamasuka kwa masiku awiri ondondozana usana ndi usiku osadya).

**ZOMWE ZILI ZONYASA KWA MUNTHU OSALA:**

1-Kuthila madzi mkamwa ndi mphuno moonjeza.
2-Kulawa chakudya popanda vuto lililonse